



MUTU 7:

UNENERI  
WOKHUDZA  
KHRISTU

---

ATAFA ELISA, MULINGU ANADZUTSA ANENERI ENA MONGA YESAYA, YEREMIYA, NDI AMOSI AMENE ANKAUZA ANTHU KUTI ASIYE MAFANO NDI MACHIMO AO. MULINGU ANKAYANKHULA KUDZERA MWA ANENERIWO, NKUMAWALEMBETSANSO MALNENERI AMBIRI A ZINTHU ZAM'TSOGOLO.

YESAYA ANALI MNENERI PA NTHAWI YA ULAMULIRO WA UZIYA, YOTAMU, AHAZI, NDI HEZEKIYA (PAFUPIFUPI 760-700 B.C.). MULINGU ANAYANKHULA KUDZERA MWA YESAYA, "NDALERA NDI KUSAMALIRA BWINO ANA ANGA, KOMA ANDIUKIRA INE. NG'OMBE YAPANGOLO IMADZIWA MWINI WAKE, KOMA ISRAELE SANDIDZIWA. NDINU MTUNDU WOCHIMWA, ANTHU ODZALA NDI MACHIMO, ANA A ANTHU OCHITA ZOIPA..."





MUKASIYA ZOIPA ZANU, NDI KUPUMUZA  
OPONDEREZEDWA, KUSAMALIRA ANA AMASIYE,  
NDI KUTHANDIZA AMAI AMASIYE,  
NDIDZAKUBWEZERETSANI M'CHIMAKE NDI  
KUKUCHIRITSANI, KOMA MUKAPANDA  
KUTEMBENUKIRA KWA INE, MUDZATHA PSITI NDI  
LUPANGA. DZIKO LANU LONSELI LIDZAKHALA  
BWINJA, NDIPO MIZINDA YANU IDZATENTHEDWA  
NDI MOTO. ADZATENGA ANA ANU ONSE KUPITA  
NAWO KU BABULO, NDIPO KUMENEKO  
ADZAFULIDWA KUTI AZIKATUMIKIRA KU NYUMBA  
YACHIFUMU YA MFUMU YA KU BABULO."






YEREMIYA ANALI MNENERI PA NTHAWI YA ULAMULIRO WA YOSIYA, YEHOYAKIMU, NDI ZEDEKIYA (PAFUPIFUPI 630-590 B.C.). ANATI, "AMBUYE AKUTI, ONANI NDAIKA NJIRA YA MOYO PAMASO PANU, NDI NJIRA YA IMFA. AMENE ADZAKHALE MUMZINDA MUNO ADZAFANA NDI LUPANGA, NDI NJALA, KOMANSO ND MLIRI: KOMA AMENE ADZATULUKAMO NAKADZIPEREKA YEKHA KWA ABABULO, AMENE AKUZINGANIWA, ADZAKHALA NDI MOYO, KOMABE ADZAKHALA KAPOLO KU BABULO. POPEZA NDIFUNA NDIONONGE MZINDAWU CHIFUKWA CHA MACHIMO AKE, AKUTERO AMBUYE: NDIDZALPEREKA M'MANJA MWA MFUMU YA KU BABULO, NDIPO MFUMUYO IDZAUTENTHA NDI MOTO."

YESAYA 1:2-4, 7, 16, 20,  
39:7; YEREMIYA 21:8-10



MULLINGU ANAYANKHULA MWA AMOSI  
KUTI, "NDIPO INE NDEMWE  
NDIDZALIMBANA NAWA NDI DZANJA  
LANGA LOTAMBASUKA NDI  
LAMPHAMVU, NDIDZAKWIYA NDIPONSO  
NDIDZAKALIPA KWAMBIRI. NDIDZAPHA  
OKHALA MUMZINDA MUNO, ANTHU NDI  
NYAMA ZOMWE: ADZAFI NDI MLIRI  
WOOPSA KWAMBIRI. NDIPO PAMBUYO  
PAKE, AKUTERO AMBUYE,  
NDIDZAPEREKA ZEDEKIYA MFUMU YA  
YUDA, NDI ANTCHITO AKE, ANTHU  
ENA, NDI ONSE OPULUMUKA KU MLIRI,  
KU LUPANGA, NDI KU NJALA,  
M'MANJA MWA NEBUKADINEZARA  
MFUMU YA KU BABULO, NDI M'MANJA  
MWA ADANI AO, NDI M'MANJA MWA





ONSE AMENE AMAFUNAFUNA MOYO  
WAO: NDIPO ADZAWAKANTHA NDI  
LUPANGA; SADZASIYA NDI MMODZI  
YEMWE WAMOYO, KAPENA  
KUWAMVERA CHIFUNDO, PENA  
CHISONI. MKWIYO WANGA Udzayaka  
NGATI MOTO NDIPO PALIBE AMENE  
ADZAUZIMITSA. ADZAKUGWIRANI  
UKAPOLO KUPITA NANU KU BABULO,  
NDIPO ADZAKUPHANI NDI LUPANGA.  
AMBIRI MWA OPITA KU BABULO  
ADZAFANA NDIPO ADZAIKIDWA  
KOMWEKO." AMOSI ANALI MNENERI  
PA NTHAWI YA ULAMULIRO WA UZIYA  
NDI YEROBOWAMU WACHIWIRI  
(PAFUPIFUPI 765-750 B.C.).

**YEREMIYA 21:5-10; AMOSI 1:4-7**



MULLINGU ANAYANKHULA MWA AMOSI,  
"AKAZI ANU ALI NGATI NG'OMBE  
ZAZIKAZI AMENE AMAFUNA KUTI AMUNA  
AO AZIWASAMALIRA BWINO KUTI  
AZIWAPATSA MKAKA.  
SIMUDZALAMULIRANSO AMUNA ANU.  
ADZAKUCHOTSANI M'DZIKO MWANU  
POKUKOLANI NDI MBEDZA KUTI  
MUKAKHALE AKAPOLO KU BABULO."



"MUDZAGONA PABWINO KWAMBIRI, MUDZADYA ZAKUDYA ZOFEWA, ZAMAFUTA. MUZIDZAMVETSERA NYIMBO UKU MUKUMWA VINYO WAMBIRI. MWATAYIRA M'FUMBI CHILUNGAMO CHANU, MWAPONDEREZA AUMPHAWI, MWAZUNZA O Lungama ndipo MWALANDIRA ZIPHUPHU, OSALUKA MWAWAMANA CHILUNGAMO. MUDZALIMA MINDA YAMPHESA, KOMA ADANI ANU NDIWO AMENE ADZAMWE VINYO WAKE. ANKHONDO ANU ADZAPHEDWA NDIPO ADZAKUGWIRANI UKAPOLO NDI KUPITA NANU KU DZIKO LACHILENDO."



## AMOSI 4-6

MULLINGU AKUTI,  
“NDIDZAONONGA MAGUWA A KU  
BETELI NDIPO NDIDZAGWETSA  
NYUMBA ZANU ZIMENE  
MUMAGWIRITSA NTCHITO PA  
NTHAWI YOZIZIRA, KOMANSO  
NYUMBA ZIMENE  
MUMAGWIRITSA NTCHITO PA  
NTHAWI YOTENTHA.

MUMAPONDEREZA OSALUKA,  
MUMALANDIRA ZIPHUPHU, NDIPO  
MUMATHUDZULA AUMPHAWI.  
NDAGWIRA MVULA KUTI ISAGWE,  
NDATUMIZA NJALA NDI  
MATENDA KOMA CHONSECHO  
SIMUKULAPA. MUMALIMA MINDA  
YAMPHESA YAMBIRI KUTI  
MUPEZE VINYO WOCHULLUKA,  
KOMASIMUDZAMWA VINYOYO.”



AMAMA, INE  
NDILI NDI  
NJALA.

753 B.C.



HOSEYA ANALI MNENERI PA NTHAWI YA ULAMULIRO WA UZIYA, YOTAMU, NDI AHAZI (PAFUPIFUPI 785-725 B.C.). IYE ANANENERA KUTI, "ISRAELE ADZAGWA NDI LUPANGA, MAKANDA AO ADZAPUMPHUNTHITSIDWA PANSI, AKAZI AO OYENBEKEZERA ADZATUMBULIDWA."

TSIKU LIKUBWERA  
LIMENE MULINGU  
ADZAKHULULUKIRA  
MACHIMO AKE, NDIPO  
ADZAKONDA ISRAELE  
KWAULERE. ISRAELE  
ADZAPHUKANSO NGATI  
DUWA. ADZAPAMBANA  
NGATI MTENGO WA OLIVI  
NDIPO ADZAKHALA WA  
FUNGO LOKOMA NGATI  
MKLINGUDZA WA KU  
LEBANONI."





M'ZAKA ZIKUBWERAZO,  
ABABULO AKADZAPITA,  
MUDZAMWAZIKIRA M'MAIKO  
A ANTHU A MITUNDU INA  
NDIPO KUMENEKO  
ADZAKUZUNZANI,  
ADZAKULANDANI KATUNDU,  
NDIPO SIMUDZAPEZA MALO  
OPUMULIRAPO."



AKUTENGA  
CHILICHONSE.  
BWANJI OSATISIYA?

AMAMA,  
TIKUPITA  
KUTI?

LIYU AKUTI AYUDA  
ONSE ADZAKHALA  
ATATULLUKA M'DZIKO  
MUNO PA MASIKU  
ATATU CHABE!

ICHI CHIKHOZA  
KUGULITSIDWA PA MTENGO  
WABWINO. SINDIWASIYA  
AYUDAWA. ATIBWERETSER  
MALONDA ABWINO  
KWABASI.

YESAYA 10:21, 35, 51:11 (627-586 B.C.); YEREMIYA 30:11;  
EZEKIELE 17:21; YOWELI 3:2; HOSEYA 13:16, 14:1-6



POTSATA ZIMENE  
ZALEMBEDWA APA, AYUDA ONSE  
AYENERA KUTULLUKA M'DZIKO MUNO  
NDIPO SIMUYENERA KUTENGA  
KANTHU KALIKONSE.

M'MBUYO  
MONSEMU NDAKHALA  
NDIKUFUNA NG'OMBE  
YONGA IYI.


POPEZA DZIKO LA ISRAELE LINAKANA  
MAU A MULLINGU, ANAYENERA  
KUMWAZIKIRA M'MAIKO ONSE A  
DZIKO LAPANSI, KOMA SANAPEZE  
MTENDERE KUFIKIRA PAMENE  
MULLINGU ANAWABWERETSANSO  
M'DZIKO LA MAKOLO AO.

"DZIKO LONSE LA ISRAELE LIDZAKHALA  
BWINJA, NDIPO MUDZATUMIKIRA  
MFUMU YA KU BABULO KWA ZAKA 70.  
KOMA ZAKA 70 ZIJA ZIKADZATHA  
NDIDZALANGA BABULO CHIFUKWA CHA  
TCHIMO LAKE, NDIPO OTSALA A  
ISRAELE NDIDZAWABWERETSA  
M'DZIKO KUTI ALIMANGENSO."



"YERUSALEMU  
ADZASIYIDWA NDIPO  
ADZATIPULIDWA NGATI  
MUNDA."







UNENERI UMENEWU  
UNAKWANIRITSIDWA.  
MDANI ADATIPULADI  
YERUSALEMU. KOMA PA  
MASIKU OTSIRIZA KACHISI  
ADZAMANGIDWANSO,  
NDIPO ANTHU  
AZIDZAKHAMUKIRA  
KUMENEKO.

MNENERI MIKA AMENE  
ADALIPO M'ZAKA ZA 750-686  
B.C., ADANENERA KUTI:



“NDIPO ADZAWERUZA ANTHU  
AMBIRI, NADZADZUDZULA MAIKO  
AMPHAMVU AKUTALI, NDIPO  
ADZASULA MALUPANGA AO  
KUKHALA MAKASU OLIMIRA, NDI  
MIKONDO YAO KUKHALA  
ZIKWANJE ZOSADZIRA: DZIKO  
SILIDZASAMULIRA LUPANGA DZIKO  
LINZAKE, NDIPO  
SADZAPHUNZIRANSO NKHONDO.  
KOMA MUNTHU ALIYENSE  
ADZAKHALA PANSI PA MPESA  
WAKE NDI PANSI PA MTENGO  
WAKE WA MKUYU; PALIBE  
CHIMENE CHIDZAWACHITITSE  
MANTHA: PAKUTI PAKAMWA PA  
AMBUYE WAMPHAMVUZONSE  
PAYANKHULA ZIMENEZI.”





“NDIPO MAIKO AMBIRI ADZABWERA, ADZATI, BWERANI, TIYENI TIPITE KU PHIRI LA AMBUYE, NDI KU NYUMBA YA MULLINGU WA YAKOBO; NDIPO ADZATIPHUNZITSA NJIRA ZAKE, NDIPOTU TIDZAYENDA M'MAKWALALA AKE: PAKUTI LAMULO LIDZATULLUKA M'ZIYONI, NDI MAU A AMBUYE KUCHOKERA M'YERUSALEMU.”

“NDIPO ADZAWERUZA ANTHU  
AMBIRI, NADZADZUDZULA MAIKO  
AMPHAMVU AKUTALI, NDIPO  
ADZASULA MALUPANGA AO  
KUKHALA MAKASU OLIMIRA, NDI  
MIKONDO YAO KUKHALA  
ZIKWANJE ZOSADZIRA: DZIKO  
SILIDZASAMULIRA LUPANGA DZIKO  
LINZAKE, NDIPO  
SADZAPHUNZIRANSO NKHONDO.  
KOMA MUNTHU ALIYENSE  
ADZAKHALA PANSI PA MPESA  
WAKE NDI PANSI PA MTENGO  
WAKE WA MKUYU; PALIBE  
CHIMENE CHIDZAWACHITITSE  
MANTHA: PAKUTI PAKAMWA PA  
AMBUYE WAMPHAMVUZONSE  
PAYANKHULA ZIMENEZI.”



“NDIPO TIDZAYENDA M'DZINA LA AMBUYE  
MULLINGU WATHU KU NTHAWI ZA NTHAWI. PA  
TSIKU LIMENELO, AKUTERO AMBUYE,  
NDIDZASONKHANITSA AMENE ADAPIRIKITSIDWIRA  
KUTALI, NDIPO NDIDZALENGA DZIKO LAMPHAMVU:  
NDIPO AMBUYE ADZAWALAMULIRA M'PHIRI LA  
ZIYONI KUYAMBIRA PAMENEPO MPAKA MUYAYA.”



YEREMIYA 25:11-12; MIKA 3:12, 4:1-7 (750-686 B.C.)

## YEREMIYA ANANENERA KUTI:

MFUMU ZEDEKIYA WACHITA ZOIPA PAMASO PA AMBUYE. SADZAPHEDWA. ADZAPITA KU BABULO KUMENE AKAKHALE MOYO WAKE WONSE PAMODZI NDI ANTHU AKE, KOMA SADZAONA BABULO NDI MASO AKE. ADZAMUCHITITSA KHUNGU. MUDZAKHALA KU BABULO KOMWEKO KWA ZAKA 70.

POTHA ZAKA 70, BABULO ADZAGONJETSEDWA NDI ASILIKALI OCHOKERA KUMPOTO NDIPO ANTHU ATHU OTSALA ADZABWERERA KU DZIKO LINO KUDZAMANGANSO MZINDA NDI KACHISI.



CHIWERUZO CHIKADZATHA,  
MULINGU ADZAKHULULUKIRA  
MACHIMO AO NDIPO MU  
YERUSALEMU MUZIDZAKHALA  
ANTHU NTHAWI ZONSE.

TENGANI BUKU ILI  
POPITA KU BABULO  
KUMENKO  
MUZIKAWERENGERA  
ANTHU. ADZIWE  
ZIMENE AYENERA  
KUPIRIRA NAZO  
ASANABWERERE KUNO.

NDIDZAKHAZIKITSANSO LUFUMU WA  
DAVIDE NDIPO INU MUDZABWERERA  
KUDZAKHALA M'DZIKO MWANU.




EZEKIELE ANANENERA  
KUTI: "ADZAMWAZIKIRA  
M'MAIKO A ANTHU A  
MITUNDU INA, KOMA  
MMENE MULLINGU  
AKUWAMWAZIRAMU, NDI  
MMENENSO  
ADZAWABWERETSERE  
M'DZIKOLI."

YEREMIYA 34:3, 51:60-61, 52:11  
(627-586 B.C.); YOWELI 3:20-21;  
AMOSI 9:11-15; EZEKIELE 12:15-16

"MULLINGU ADALONJEZA ABRAHAMU KUTI MBEU  
YAKE IDZALANDIRA DZIKO MPAKA KALEKALE,  
NDIPO KUTI SADZAPHWANYA PANGANO LAKE.  
KOMABE, ANTHU AKACHIMWA, MULLINGU  
AMAWATUMIZA NGATI AKAPOLO M'MAIKO ENA  
KUMENE AMAKATUMIKIRA MILLINGU  
YACHILENDO, KOMA PAMBUYO PAKE  
AMAWABWERETSANSO M'DZIKOLO."





"IGUPTO ADZALANGIDWANSO  
NDI ABABULO, NDIPO KWA ZAKA  
40 IGUPTO ADZAKHALA BWINJA.  
AKADZABWERAKO KU BABULO,  
IGUPTO SADZAKHALANSO  
WAMPHAMVU MONGA KALE,  
KOMABE ADZAPIRIRA MPAKA KU  
MAPETO. NDIPO PA MASIKU A  
KUTSOGOLOKO IGUPTO NDI  
ASIRIYA ADZALUMIKIZANA NDI  
ISRAELE ANTHU ANGA, MAGULLU  
ATATUWA ADZACHITA  
MGWIRIZANO WAMTENDE, NDIPO  
INE NDIDZAWADALITSA"





"AFILISTI ADZAONONGEDWA NDIPO  
ADZATHERATU PSITI. MOMWEMONSO,  
ASIDODI, EKRONI, NDI AMONI  
ADZATHERATU. EDOMU ADZAKHALA BWINJA  
LENILENI. TURO ADZAONONGEDWA NDIPO  
MIYALA NDI MATABWA AKE ZIDZATAYIDWA  
M'NYANJA. ANTHU SADZAKHALAMONSO  
NDIPO NTHAKA YAKE IDZAKHALA YOSALALA  
NGATI MWALA, KUKHALA NGATI MALO  
AMENE ASODZI AMAYALAPO UKONDE WAO."

"KOMA PERISIYA (IRANI),  
TURKEY, ETIOPIYA, NDI LIBIYA  
ADZAKHALAPO MPAKA  
MUYAYA, ADZAYESETSA  
KUCHITIRA CHIWEMBU DZIKO  
LA ISRAELE, KOMA ADZAFERA  
PA MAPIRI A ISRAELE."





BAIBULO SILIPHOPHONYA PA MAULOSI AKE.  
MIZINDA NDI MAIKO AMENE ANENERI ADANENA  
KUTI ADZATHA, ADATHADI. MAIKO AMENE ANENERI  
ADATI ADZAKHALAPO ALIPOBE MPAKA LERO LINO.

EZEKIELE MUTU 25, 26:15-19, 29:12-16,  
30:1-8; YEREMIYA 25:15-26; AMOS 1

M'CHAKA CHA 605 B.C.  
ISRAELE ANAGONJETSEDWA  
NDI ABABULO, MONGA  
MOMWE ANENERI ADALOSERA.



INU AMBUYE,  
CHIFUKWA CHA MACHIMO A  
MAKOLO ATHU TIKULANGIDWA.  
TITHANDIZENI KUTI TIZIMVERA  
MALAMULO ANU NGAKHALE  
M'DZIKO LACHILENDO  
LINO.




DANIELE ANALI MKAIDI M'DZIKO LACHILENDO,  
KOMA ANASANKHA KUKHALA WOKHULLUPIRIKA  
KWA MULLINGU WAKE. AMENE  
ANKAMUYANG'ANIRAWO ADAONA KUTI DANIELE  
ANALI NDI MTIMA WABWINO, CHONCHO  
ADAMPATSA UDINDO WINA NDIPO TERE ANALI  
MMODZI MWA ANTHU ANZERU A KU BABULO.



TIKUKUTHOKOZANI,  
INU AMBUYE WAKUMWAMBA  
NDI DZIKO LAPANSI, MFUMU  
YA DZIKO LONSE, POPEZA  
MUMAPEREKA CHAKUDYA  
KUCHOKERA M'NTHAKA.


DANIELE ANALI MKAIDI M'DZIKO LACHILENDO,  
KOMA ANASANKHA KUKHALA WOKHULLUPIRIKA  
KWA MULLINGU WAKE. AMENE  
ANKAMUYANG'ANIRAWO ADAONA KUTI DANIELE  
ANALI NDI MTIMA WABWINO, CHONCHO  
ADAMPATSA UDINDO WINA NDIPO TERE ANALI  
MMODZI MWA ANTHU ANZERU A KU BABULO.





NEBUKADINEZARA, MFUMU  
YA BABULO, ANADZIDZIMUKA  
USIKU CHIFUKWA CHA  
MALOTO ODABWITSA.

ZIMENEZI ZIKUTANTHAUZA  
CHIYANI? ZEDI, MALOTO OTERE  
AMADZA NDI MILINGU POFUNA  
KUULULA ZAKUTSOGOLO




INU NDINU  
ANTHU ANZERU. MUMATI  
MILINGU IMAKUUZANI ZINTHU.  
CHONCHO MUNDIUZE ZIMENE  
NDINALOTA NDIPONSO  
TANTHAUZO LAKE.

KOMA  
TINGAKUUZENI  
BWANJI TANTHAUZO LA  
MALOTO ANU POPANDA  
KUTIUZA MALOTOWO?  
PALIBE AMENE ANGATERO  
KUPATULA MILINGU  
YOKHA.

DANIELE 1:2-7, 17-21, 2:1-11






NDIMADZIWA KUTI  
NONSENU NDINU ABODZA.  
MILINGU SIYANKHULA NANU.  
NONSENU MUPHEDWA PAMODZI NDI  
MABANJA ANU, NDIPO NYUMBA  
ZANU ZISANDUKA KOTAYIRAKO  
ZINYALALA.

PEPA DANIELE, KOMA  
MAWA IWE PAMODZI NDI ANZERU  
ANZAKO A BABULO MUDZAPHEDWA.  
MFUMU SIKUKHULUPIRIRA NGAKHALE  
ANSEMBE AKE OMWE.



KOMA **YEHOVA** MULINGU  
AKHOZA KUULULA LOTO LA  
MFUMU NDI TANTHAUZO LAKE.  
NDIPEMPHERE PANDEKHA.  
YESANI KUMUPEMPHA KUTI  
ADIKIRE KWA TSIKU LIMODZI.

A man with extensive tattoos on his arms and back is kneeling on a stone floor, his head bowed in prayer. He is wearing a dark tank top and shorts. In the background, a bright, glowing yellow light emanates from a wall, and a white, ethereal silhouette of a man in a long coat stands within this light. The scene is set in a dark, possibly underground or cave-like environment.


AMBUYE, INU  
NOKHA NDIYE MULLINGU  
NDI MFUMU YA DZIKO  
LONSE. CHONDE  
MUONETSENI MTUMIKI  
WANU ZINTHU  
ZAKUTSOGOLO. KULIBE  
MULLINGU WINA KOMA  
INU NOKHA.

**DANIELE,  
TANDIMVERA....**



**FULUMIRANI,  
MUPITE NANE  
KWA MFUMU!**


**NGATI SUKAIWUZA  
MFUMU LOTO LAKE,  
AKANDIPHAKO INE  
KUMENEKO.**



INU MFUMU,  
NDINU MFUMU YA  
MAFUMU ONSE  
CHIFUKWA MULLINGU  
WAKUMWAMBA NDIYE  
WAKUCHITIRANI.  
WAKUPATSANI INU  
MASOMPHENYA A  
ZIMENE ZIDZACHITIKE  
M'TSOGOLOMO.

USANDITAIRE NTHAWI.  
KODI UKHOZA KUNDIENZA  
MALOTO ANGA KAPENA AI?

MULLINGU WOONA,  
MLENGI WA DZIKO LONSE,  
WALLULA MALOTO ANU  
KWA MTUMIKI WANU.



INU MFUMU,  
MUNAONA MASOMPHENYA  
A CHOLUMBA CHACHIKULU.  
CHOLUMBA CHIMENECHI  
CHIKUIMIRA UFUMU WANU  
NDI MALUFUMU ENA ATATU  
AMENE ADZATSATIRE.

NDI ZONADI!  
SINDINAUZE  
ALIYENSE!  
MULLINGU WAKO  
YEKHA NDIYE  
MULLINGU.




INUYO NDINU  
MUTU WA GOLIDE.  
MUSANAGONJETSE YUDA,  
ANENERI ATHU ANKATIENZA  
KUTI ADZATILANGA  
CHIFUKWA CHA MACHIMO  
ATHU NDIPO ADZAPATSA  
INU UFUMU. CHONCHO  
UFUMU WANU UDZAKHALA  
WAULEMERERO.




NGANGA YASILIVA  
IKUIMIRA UFUMU WINA,  
AMEDI NDI APERISIYA. INUYO  
MUKADZAFU, IWOWA  
ADZAGONJETA BABULO NDIPO  
ADZALAMULIRA DZIKO LONSE  
MONGA MUKUCHITIRA INUMU.






INU MFUMU. PAMBALI  
PA MUTU WAGOLIDE NDI NGANGA  
YASILIVA, MUNAONANSO MIMBA  
YAMKUWA. MKUWAWO UKUIMIRA  
UFUMU WACHITATU, AGRIKI.  
UDZABWERA PAMBUYO PA APERISIYA  
NDIPO UDZAKHALA WAMPHAMVU  
NDI WOOPSA.


UFUMU WACHINAI UDZAKHALA  
WOSIYANA NDI MAUFUMU ENAWO,  
MIYENDO YAKE IDZAPANGIDWA NDI  
CHITSULO, NDIPO UDZASINDIKIZA NDI  
KUPHWANYA MAIKO AMBIRI. KOMA  
MUNAONA KUTI ZALA ZACHITSULO  
ZINAPHATIKIZANA NDI DOTHI. PA  
MASIKU OTSIRIZA UFUMUWO  
UDZAGAWIKA PAKHUMI,  
CHONCHO UDZAFOOKA.




KUONJEZA APO,  
INU MFUMU, MUNAONA  
MWALA UTATSAKAMUKA  
KUCHOKA M'PHIRI, MUNTHU  
OSAIKANKHA KONSE.  
UNAKUNKHUNIZIKA KUCHOKERA  
M'PHIRI MUJA MPAKA  
KUDZAMENYA MAPAZI A  
CHOLIMBA CHIJA NDI  
KUONONGA MAUFUMU  
ONSE M'KAMPHINDI  
KOCHEPA.



MWALA  
UMENEWO  
UKUIMIRA MWANA  
WA MULLINGU  
AMENE  
ADZABWERA PA  
DZIKO LAPANSI  
KUDZAKHAZIKITSA  
UFUMU  
WAULEMERERO.




PA KUTHA KWA NTHAWI,  
AKUFA ONSE ADZAUKITSIDWA  
KUTI AKAIMÉ KU CHIWERUZO. IWO  
AMENE ADACHITA ZOIPA ADZALANDIRA  
MANYAZI NDI CHITONZO CHOSATHA.  
IWO AMENE ADACHITA ZABWINO  
ADZALANDIRA MOYO WOSATHA.



MOSAKAIKA KONSE, MALI  
AMENE UKUYANKHULA NGOCHOKERA  
KWA MULLINGU. WATHA BWANJI KUDZIWA  
MALOTO ANGA CHOTERE? NDIKUPATSA  
LIDINDO WOYANG'ANIRA  
ANZERU ONSE.

DANIELE ANAKHALA M'DZIKO LA BABULO KWA  
ZAKA 68. ANATANTHALUZIRA MALOTO AMBIRI  
NDIPONSO ANKALOSA ZAKUTSOGOLO NTHAWI  
ZAMBIRI. POSAKHALITSA, NEBUKADINEZARA  
ANAMWALIRA NDIPO MWANA WAKE BELISAZARA  
ANALOWA LIFUMU M'MALO MWAKE.



USIKU WINA PAMENE BELISAZARA ANKACHITA  
PHWANDO, DZANJA LODABWITSA LINAONEKA  
NDIPO LINALEMBA PA KHOMA. DANIELE  
ADAITANIDWA KUTI AKATANTHAUZIRE  
ZIMENEZI. MULLINGU ADAMPATSA NZERU  
ZODZIWIRA CHIYANKHULO CHOSADZIKACHO.

INU MFUMU,  
MWACHIMWIRA MULLINGU.  
MONGA ANENERI ADALOSERA,  
UFUMU WANU WALANDIDWA USIKU  
WOMWE UNO NDIPO WAPEREKEDWA  
KWA AMEDI NDI APERISIYA.

MLALIKI 12:13-14; YESAYA  
9:6-7, 45:1; DANIELE  
2:34-35, 44-48; 5:1-29;  
CHIVUMBULUTSO 20:11-21:5

ANENERI ADALOSA KUTI MDANI AMENEYU  
ADZAFIKA MWACHINSINSI PODUTSIRA PA  
ZIPATA ZIWIRI PAMENE PANKADUTSIRA  
MADZI OLOWA MU MZINDA. AYENERA KUTI  
ABABULO ANALI ATALEDZERA KWAMBIRI  
CHONCHO SANAONE ADANIWO. MBIRI  
IMALONGOSOLA MOMWEMU KUTI ABABULO  
ADAGONJETSEDWA MOTEREMU.






AMEDI NDI APERISIYA ATAGONJETSA ABABULO,  
DANIELE ADAPEZA BUKU LAKALE LOLEMBEDWA NDI  
MNENERI YEREMIYA, LIMODZI MWA MABUKU A  
M'BAIBULO. PAMENE ANKALIWERENGA, ANADZIDZIMUKA  
POONA KUTI MULLINGU ANANENA KALE KUTI UKAPOLO  
WA KU BABULO Udzatha pakadzapita zaka 70.




PAMBUYO PAKE OTSALA ADZABWERERA KU YERUSALEMU NDI KUKAMANGANSO MALINGA AKE NDI KACHISI. POPITIRIZA KUWERENGA, ADAPEZA KUTI ZAKA 200 M'MBUYOMO MNENERI YESAYA ADANENA NGAKHALE DZINA YA MFUMU YA KU PERISIYA IMENE IDZALAMULA KUTI AYUDAWO ABWERERE KWAO.






TSOPANO PAFUPIFUPI  
ZAKA 69 ZAPITAPO...CHATSALA  
NDI CHAKA CHIMODZI CHOKHA. AKUTI  
KORESI NDIYE MTUMIKI WA MULUNGU,  
WOCHITA CHIFUNIRO CHA MULUNGU.  
ADZALAMULA KUTI TIBWERERE KU  
DZIKO LATHU! WODALITSIKA NDINU,  
INU AMBUYE MULUNGU WATHU,  
MFUMU YA DZIKO LONSE.



M'CHAKA CHA 70 CHA UKAPOLO, KORESI ADAMASULA  
AYUDA, MONGA MOMWE MALEMBO OYERA  
ADANENERATU. AYUDA OPOSA 52,000 ANABWERERA  
KWAO KUKAMANGANSO MZINDA WA YERUSALEMU.

MONGA MOMWE MULLINGU  
ADALONJEZERA ABRAHAMU, IYE WATIPATSA  
DZIKOLI NGATI CHUMA CHATHU CHAMUYAYA.  
ADACHENJEZA MAKOLO ATHU KUTI ADZATIPEREKA  
M'MANJA MWA ADANI ATHU, TIKADZATUMIKIRA  
MILINGU INA, KOMANSO ADALONJEZA KUTI  
SADZAIWALA ANTHU AKE. MULLINGU WAKWANIRITSA  
MAU AKE. TSOPANO POTI TABWERERA KWATHU,  
TIYENERA KUMVERA MULLINGUYO.



TIKONZEKERE  
BWINO. TIMANGA  
MALINGA POYAMBA  
NDIPO KENAKA  
TIYAMBA KACHISI.

INU AMBUYE  
MULINGU WA ABRAHAMU,  
MWATIBWERETSANSO KU  
DZIKO LATHU. TIPHUNZITSENI  
KUYENDA M'NJIRA ZANU.

NDABWERETSA  
MADZI AWA. TIYENI  
TIYAMBEPO KUGWIRA  
NTCHITO.

DANIELE 9:1-2; YEREMIYA  
25:11-12, 29:10

DANIELE ANAKALAMBA KWAMBIRI, CHONCHO  
SANABWERERE NAWO ANZAKE AJA. KOMABE  
ANKAGWIRA NTCHITO YOTAMANDIKA YOLANGIZA  
MAFUMU A AMEDI NDI PERISIYA, AMENE  
ANKAKHALA MU MZINDA WA BABULO PA NTHAWI  
IMENEYO. MULUNGU ADAMPATSA  
MASOMPHENYA AMBIRI A ZAKUTSOGOLO,  
MPAKA MASOMPHENYA ONENA ZA KUTHA KWA  
NTHAWI YA PANSI PANO. PA MALOTO AKE ENA  
ANAONA CHILOMBO CHA CHACHITSULO.  
MNGELO ADAMUZA TANTHALIZO LA  
CHILOMBOCHO.






MULINGU AKUKUONETSA  
ZIMENE ZIDZACHITIKA PA  
MASIKU OMALIZA. ADAULULA KWA  
NEBUKADINEZARA KUTI PADZAKHALA  
MAUFUMU ANAI. TSOPANO PAONEKA  
KALE MAUFUMU AWIRI. UFUMU UWU  
WA AMEDI NDI APERISIYA UKADZATHA,  
AGRIKI ADZABWERA. UFUMUWO  
UDZAGONJETSA MWAMPHAMVU KOMA  
SUDZAKHALITSA CHIFUKWA UDZAGAWIKA  
PANAI, NDIPO A MU UFUMUWO  
AZIDZAMENYANA OKHAOKHA MPAKA  
PADZATSALA MAUFUMU  
AWIRI OKHA.



MAUFUMU  
AWIRIWO ADZAGONJETSA  
MAIKO MOLAPITSA KWA ZAKA  
ZAMBIRI MPAKA PAMENE  
ADZAGONJETSEDWE NDI UFUMU  
WACHINAI, NDIPO CHILOMBO  
CHACHITSULOCHO CHIKUIMIRA  
UFUMU WACHINAIWU.




UFUMU WACHINAI  
UDZAKHALA NGATI CHITSULO,  
WAMPHAMVU NDI WOOPSA  
KWAMBIRI KUPOSA MAUFUMU  
A M'MBUYOMO. UDZAGONJETS  
ONSE, KOMA PA MASIKU  
OMALIZA UFUMUWU UDZAGAWIKA  
PAKHUMI. TSONO  
PADZABWERA MUNTHU AMENE  
AZIDZAYANKHULA ZA MTENDERE.  
IYEYU NDIYE NYANGA YOMALIZA  
YOMERA PAMUTU PA  
CHILOMBO.



PA MASIKU OMALIZA,  
IYEYO ADZANYENGERERA  
ANTHU NDIPO AZIDZALONJEZA  
MTENDERE, KOMA M'MALO  
MWAKE AZIDZANGOGONJETA  
ANTHUWO NDI KUWAONONGA.  
ADZAIKA ZINTHU ZONYANSA  
M'MALO OYERA, M'KACHISI WA  
AYUDA, KUTI KACHISIYO AKHALE  
ODETSEDWA MONGA MWA  
MIYAMBO YA AYUDA, KUTI  
TSONO ALEKE KUPEREKERAMO  
NSEMBE. NDIYENO PADZAFIKA  
NTHAWI YA MASAUTSO  
AAKULU PA DZIKO LONSE  
LAPANSI, KOMA  
OLUNGAMA  
ADZAOMBOLEDWA.



DANIELE, MULLINGU AFUNA  
KUKUONETSA ZIMENE  
ZIDZACHITIKA NDI NTHAWI YAKE  
IMENE ZIDZACHITIKIRE.  
KUCHOKERA PA NTHAWI IMENE  
LAMULO LOTI ANTHU  
ABWERERE NDI KUKAMANGANSO  
KACHISI LAPEREKEDWA,



PADZAPITA ZAKA 483,  
NDIPO PAMBLIYO PAKE  
MESIYA ADZAPHEDWA POLIPIRA  
MACHIMO A ANTHU ONSE,  
NDIPO KENAKA KACHISI  
ADZAONONGEDWANSO.

LINENERI UWU UDZAKWANIRITSIDWA, NDIPO  
MESIYA ADZADZOWEDWA. MACHIMO  
ADZAKHULLULUKIDWA, NDIPO ANTHU  
ADZAPATSIDWA KULLINGAMA KOSATHA.

MONGA MOMWE DANIELE ADALEMBERA,  
MESIYA ADALOWA MOPAMBANA MU  
YERUSALEMU PA TSIKU LOMWE ZAKA 483 ZIMATHA.





MULLINGU ADAUZA ADAMU NDI HAVA KUTI MBEU YA MKAZI IDZABWERA KUDZAONONGA WOIPAYO. ADAUZA NOWA KUTI MESIYA ADZABWERA KUCHOKERA M'BANJA LA SEMU, OSATI YAFETE KAPENA HAMU. MULLINGU ADAUZA ABRAHAMU KUTI MPULUMUTSI ADZACHOKERA MWA ZIDZUKULU ZAKE KUPYOLERA MWA ISAKE MWANA WAKE. MULLINGU ADAUZA ISAKE KUTI WOLONJEZEDWAYO WAKE, NDIPO ADAUZA YAKOBO KUTI KHRISTU ADZACHOKERA MWA YUDA.

GENESIS 49:9-10; SALIMO 22, 53; YESAYA 7, 9:1-2, 42:1,  
49:6, 53; DANIELE 9:25-26; MIKA 5:2; ZEKARIYA 9:9;  
MATEYU 24:1-2; AHEBRI 2:9

MULINGU ANAPERKA KWA ANENERI MALNENERI  
AMBIRI ACHINDUNJI ONENA ZA MOYO WA MPULUMUTSI  
WOLONJEZEDWAYO. AMATI NGWACHIKHALIRE, KUTI ADZABADWA  
MWA NAMWALI MU MZINDA WA BETELEHEMU WA YUDA,  
ADZAKHALA WODZICHEPETA M'MAKHALIDWE AKE, NDIPO  
ADZAKHALA WOFATSA NDI WOKWERA PA BULU. AMBUYE ADZAIKA  
MZIMU WAKE PA IYE, NDIPO ADZAWERUZA ANTHU A MITUNDU  
INA. ADZAKHALA KUWALA KWA ANTHU A MITUNDU INA NDIPO  
ADZABWERETA CHIPULLUMUTSO KWA ANTHU ONSE A PA DZIKO  
LAPANSI. ADZAKHALA MESIYA WOZUNZIKA NDIPO ANTHU AKE  
ADZAMUKANA, NDIPONSO ADZAFAPOKHOMEDWA MANJA NDI  
MAPAZI AKE. ADZAMUKWEZA PA MTANDA ALI WAMALISECHE  
NDIPO ADZAMVA LUDZU, KOMA M'MALO MWAKE ADZAMPATSA  
VINYO WOSASA KUTI AMWE. ADZAFERA PAKATI PA MBAVA  
NDIPO ADZAIKIDWA M'MANDA A MUNTHU WOLEMERA.

MAULOSI A DANIELE OKHUDZA MAUFUMU ANAI  
ANAKWANIRITSIDWA MONGA MOMWE ADALOSERA.  
M'CHAKA CHA 330 B.C. ALEKSANDRO WAMKULU,  
WOCHOKERA KU GRISI, ANAYAMBA KUONETSA MPHAMVU  
ZAKE KWA ZAKA 7, NDIPO ANAGONJETSA MAIKO AMBIRI,  
KUPHATIKIZAPO UFUMU WA AMEDI NDI APERISIYA. GRISI  
ANAKHALA WAMPHAMVU MPAKA PAFUPIFUPI CHAKA CHA  
167 B.C. POMWE UFUMU WACHINAI, ROMA, ANAYAMBA  
KUGONJETSA MAUFUMU ENA.

PA MALOTO A NEBUKADINEZARA, ROMA ANKAIMIRA  
MAPAZI NDI MIYENDO YACHITSULO, NDIPO  
M'MASOMPHENYA A DANIELE, ROMA ANKAIMIRA  
CHILOMBO CHACHITSULO CHIJA, CHIMENE CHINAKUZA  
MPHAMVU ZAKE NDI KUGONJETSA MAIKO AMBIRI, MONGA  
MOMWE MNENERI ADALOSERA. M'CHAKA CHA 5 B.C.,  
ROMA ANKALAMULIRA ISRAELE NDI DZANJA LACHITSULO.

# ***PATAPITA ZAKA 500***

ZAKA ZOPOSA 500 ZINAPITAPO KUCHOKERA PA MAULOSI  
A DANIELE. M'CHAKA CHA 6 B.C. AROMA ADAPATSA  
AYUDA UFULU WA CHIPEMBEDZO KOMA ANKAWAKHOMETSA  
MSONKHO WAKULU KWAMBIRI. KACHISI  
ADAAMANGIDWANSO NDIPO ANALI NGATI MTIMA WA MOYO  
WA AYUDA. AMBIRI ADAIWALA MALINENERI OKHUDZA  
ZA KUBWERA KWA MESIYA, KOMA ENA ANKASUNGABE  
MALAMULO NAMAYEMBEKEZA KUBWERA KWA KHRISTU.  
MMODZI MWA IWO ANALI MUNTHU WINA  
WOKALAMBA WOTCHEDWA SIMEONI.

ANALI MUNTHU WOYERA MTIMA  
AMENE ANKAFUNITSITSA ATAONA UJA AMENE ANENERI  
ADAKAMBA ZA IYE. KWA ZAKA ZAMBIRI ANKAWERENGA  
MALNENERI NDIPO ADAZINDIKIRA KUTI NYENGO YA MESIYA  
IKUYANDIKIRA. KOMA TSOPANO ANALI WOKALAMBA  
NDIPO MASIKU A MOYO WAKE ANKACHEPERACHEPERA.  
ZAKA 4,000 ZINAPITAPO KUCHOKERA PAMENE MULLUNGU  
ADALONJEZA HAVA KUTI MBEU YAKE IDZABWERA  
KUDZAONONGA NTCHITO ZA WOIPAYO.

***NTHAWI INALI ITAKWANA TSOPANO.*** MALULOSI  
OPOSA 350 ANAYENERA KUKWANIRITSIDWA.



<https://goodandevilbook.com/>